
# MASOMPHENYA ADZIKO LA MALAWI



*Dziko Lodzidalira Komanso Lotukuka Pachuma Mokomera Aliyense*

MALAWI 2063

# Masomphenya Athu

**'Dziko lodzidalira komanso lotukuka pachuma mokomera aliyense'**

## Zomwe Tagwilizana Ngati A Malawi

'Ife monga a Malawi tagwilizana kuti dziko lathu litukuke pankhani zachuma ndi mafakitale pofika chaka cha 2063 ndi cholinga choti tikhale odzidalira patokha pa ntchito zachitukuko mosadalira kwambiri mayiko ndi mabungwe akunja. Mafakitale athu makamaka adzakhala amphamvu komanso olumikizana ndi za ulimi, za migodi ndi magawo ena a zachuma. Tidzakwanilitsa masomphenya athuwa pogwira ntchito limodzi molimbika ngati a Malawi ndipo sitidzalora kuti wina atisokoneze'.

## Malawi Yemwe Tikumufuna Pofika Chaka Cha 2063

1. Dziko lotukuka komanso lodzidalira pa ntchito zachuma ndi zamafakitale pofuna kudzipezera patokha zofunika pa chitukuko cha dziko lathu;

2. Dziko lotukuka kwambiri komanso lokhala ndi ntchito za makampani ndi mafakitale amphamvu motsogozedwa ndi ntchito za ulimi wapamwamba ndi migodi;

3. Mizinda ndi matawuni apamwamba ndi malo antchito zokopa alendo okhala ndi zipangizo zonse zoyenera kuti anthu akhale ndi miyoyo yapamwamba;

4. Anthu ogwilizana, amtendere, okonda dziko lawo, okhulupilira mukuthekera kwa mphamvu zawo, ndinso okangalika pakutukula dziko lawo;

5. Dziko lokhala ndi ndondomeko zoyenera za ulamuliro wabwino komanso mabungwe amphamvu olondoloza kuti malamulo a dziko akutsatidwa mokomera aliyense;

6. Anthu ogwira ntchito za boma modzipereka ndi mwaukadaulo;

7. Ntchito za makampani ndi zina zomwe si zaboma zochuluka komanso zapamwamba;

8. Ntchito zamagetsi, zamtengatenga ndi mtokoma, za lamya, ndinso zina zonse zomangamanga zopititsa patsogolo chuma chathu molingana ndi mayiko ena otukuka kwambiri pa dziko lapansi;

9. Anthu ogwira ntchito okhala ndi kuthekera komanso ukadaulo molingana ndi mayiko ena otukuka kwambiri pa dziko lapansi;

10. Chilengedwe chosamalika posayang'anira kupanga chuma chathu chalero, koma mokomera ana athu ndi mibado yamtsogolo.

# Kutambasula Masomphenya Athuwa Mwachidule

A Malawi talankhula. M'masomphenya athuwa, omwe tikuwatcha 'Malawi 2063' (MW2063), tikufuna kusintha dziko lathuli kukhala lotukuka ndiponso lodzidalira pa chuma, makamaka pa ntchito za mafakitale pofika chaka cha 2063.

Pakadali pano, kafukufuku akusonyeza kuti chuma cha dziko lino chitamakwera ndi 6 percent chaka chilichonse, ambiri mwa ife titha kumadzapeza ndalama zosachepera chikwi chimodzi cha dollar ya ku America (US$1,000) pachaka pofika chaka cha 2030. Kunena mwatchutchu, ngati dziko la Malawi litadzipereka pogwila ntchito zake za chitukuko ndi kukweza maluso osiyana-siyana, likhoza kutukuka mofulumira, a Malawi ambiri mkumapeza ndalama zosachepera zikwi zinayi za dollar yaku America (US$4,000) pa chaka tisanafikenso chaka cha 2063.

A Malawi ambiri ochokera madera osiyanasiyana, kuphatikizilapo omwe ali kunja kwadziko lino, anayikapo maganizo awo pomwe masomphenya awa amakonzedwa. Malawi 2063 akufotokoza zofuna ndi zolinga za a Malawi pofika chaka cha 2063. Masomphenya awa akhazikika pangodya zitatu:

1. Ulimi wamakono, opindula komanso wamalonda;

2. Ntchito za mafakitale ndi migodi;

3. Kukhala ndi mizinda yapamwamba m'madera osiyana-siyana a m'dziko lino, kuphatikizapo ku malo okopa alendo.



Masomphenyawa akufotokozanso mwatsatane-tsatane zinthu zofunikira zomwe ziyenera kukhala m'malo kuti dziko la Malawi likhale lodzidalira, lopanga chuma mokomera aliyense, komanso kuti m'Malawi aliyense akhale ndi moyo otukuka.

Ngati dziko, takhala tikutsatila kwambiri ndondomeko za kayendetsedwe ka chuma zochokera kumaiko akunja zomwe nthawi zina sizigwirizana ndi mavuto omwe dziko lathu limakumana nawo.

Kafukufuku akutsimikiza kuti dziko lathu litha kusintha ngati titakhazikika pa ntchito yothana ndi mavuto omwe tikukumana nawo kusiyana ndikumangodandaula kapena kumangotengera zomwe mayiko ena akuchita.

Cholinga chathu m'masomphenya awa ndi kusintha kaganizidwe kathu ndi kuyamba kukhulupilira kuti patokha tikhoza kutukula dzikoli. Kwa nthawi yayitali takhala tikudalira thandizo ndi ngongole zochokera ku mayiko ndi mabungwe akunja kuti tipeze ndalama zothandizira chitukuko cha dziko lathuli.

Chofunitsitsa chathu padakali pano ndi kukonza njira zabwino zopezera chuma kuti dziko lathu likhale lodzidalira pa ntchito za chitukuko, ndipo kuti ngongole zizitengedwa pokhapokha chuma chathu chapelewera pa zitukuko zikulu-zikulu komanso zofunika kwambiri.

Pofika chaka cha 2063, tidzakhala ndi dziko lachuma chokhazikika chothandizira kupititsa patsogolo ntchito zathu za chitukuko. Chaka cha 2063 chinasankhidwa chifukwa dziko la Malawi lidzakhala litakwanitsa zaka 100 za ufulu odzilamulira palokha. Masomphenya athu akuyang'ana ku zaka zambiri pofuna kutukula dziko lathu ndi miyoyo yathu, kuphatikizapo mibado yamtsogolo. Tikufuna kuti pogwira ntchito zachitukuko, tisamaganizile kuti ife tipindula chani koma tidzilingalira za chitukuko chomwe tidzasiyile ana athu ndinso ana awo.

***Pofika chaka cha 2063, tidzakhala ndi dziko lachuma chokhazikika chothandizira kupititsa patsogolo ntchito zathu za chitukuko***

Tikulakalaka kuti podzafika chaka cha 2063, ana athu adzakhale pa ufulu weniweni pa ntchito za chuma ndi chitukuko. Ndipo tikufunitsitsa kuti ana athu azidzayenda monyadira ku mayiko ena padziko lonselino lapansi pozindikila kuti sakudaliranso ena pa ntchito za chitukuko ndi moyo wawo wa tsiku ndi tsiku.



Anthu ambiri m'dziko lathuli ndi achinyamata, kotero achinyamata ayenera kupatsidwa mpata woyenera komanso kukhala okangalika pa ntchito zonse za chitukuko kuti dziko lathu lipite patsogolo.

Kusintha kwa dziko lathu kuli pa magawo awiri: poyamba, tikufuna kusintha malankhulidwe ndi maganizidwe athu posiya kukhazikika pa zaumphawi wathu ndipo kuti m'malo mwake, tizikhazikika pa momwe tingapangire chuma chochuluka kuti tizidzidalira patokha.

Kachiwiri, tikuyenera kukonzanso ntchito za chuma m'dziko lino popititsa ntchito za mafakitale ndi kumapanga katundu wambiri wogulitsa kunja m'malo momangoyitanitsa chilichonse kuchokera ku mayiko ena.

Ntchito za chitukuko chimenechi zidzatsogozedwa ndi a Malawi eni ake pofuna kumanga dziko lawo ndi kudzidalira pa ntchito zonse za-chuma, kuphatikizapo za mafakitale ndi ulimi wapamwamba. Tidzayenda limodzi ngati a Malawi ndi cholinga chimodzi kufikila Malawi yemwe tonse tikumufuna titamupeza. Ngati dziko la Malawi, tikuzindikila kuti pali ndondomeko zina za chitukuko za m'maiko a mu Africa komanso dziko lonse lapansi zomwe masomphenya athu akhalenso akutsamilapo. Mwachitsanzo, masomphenya athu adzilumikizananso ndi mfundo za chitukuko za dziko lonse lapansi zotchedwa Sustainable Development Goals (SDGs); Agenda 2063, yomwe yimatambasula za Africa wotukuka yemwe timamufuna; komanso mfundo za chitukuko za mayiko ozungulirana nawo omwe tili nawo limodzi ngati ma membala a Southern Africa Development Community (SADC) ndi Common Market for Eastern and Southern Africa (COMESA).

***Tidzayenda limodzi ngati a Malawi ndi cholinga chimodzi kufikila Malawi yemwe tonse tikumufuna titamupeza***

Pozindikila kuti masomphenya athu ndi otenga nthawi yayitali kuti tiwafikile, ndondomeko zina zazifupi monga za zaka khumi komanso za zaka zisanu zizipangidwa pomwe tikugwira ntchito zotifikitsa ku masomphenya athu a chaka cha 2063.


Pamene masomphenya athuwa amapangidwa, tinali ozindikira kuti ntchito zina zandale zakhala zikutilepheretsa kusintha magwilidwe antchito za chitukuko komanso maganizidwe athu. Kotero, kuti tifikile masomphenya ofuna kutukula dziko lathuli, tikulimbikitsa anthu onse andale kuti akhale patsogolo kumema anthu onse ndi mabungwe kuti agwilire ntchito pamodzi ndi boma.

Tikufunanso kuti atsogoleri akhale patsogolo kuphunzitsa anthu kuti ndale zokha, popanda kugwira ntchito, sizingathandize kutukula dziko lino, koma kuti atsogoleri onse athandizire kuti masomphenya athuwa tiwafikile.

***Tikufunanso kuti atsogoleri akhale patsogolo kuphunzitsa anthu kuti ndale zokha, popanda kugwira ntchito, sizingathandize kutukula dziko lino***

Tikufuna atsogoleri osakomedwa ndi maudindo koma kulimbikira kuti zofuna za a Malawi zikwanilitsidwe pogwilitsa ntchito bwino maudindo omwe adapatsidwa. Ngati atsogoleri atachita izi, a Malawi adzazindikila kuti pakufunika kugwila ntchito molimbika pawokha pofuna kupeza zomwe akufuna ndi kusiya khalidwe lopembedza anthu omwe ali m'maudindo kuti alandire zaulere.






Tidzaziwa kuti tayamba kudzidalira patokha ngati dziko pamene tidzayambe kumachita zitukuko zambiri pogwiritsa ntchito ndalama zathu osati zochokera ku mabungwe ndi mayiko akunja kapena ngongole. Komanso pomwe tidzasiye kudalira kufuna kwabwino kwa anthu ena pa za chuma ndi chitukuko m'makomo mwathu.

Motsindikiza, tizadziwanso kuti ndife odzidalira pa tokha tikadza-wona kuti madera onse adziko lino ali ndi zonse zofunikira pa mi-yoyo ya anthu, monga: chakudya chokwanila komanso chamagulu kwa munthu wina aliyense chaka chonse; zipatala zomwe zili ndi mankhwala, ogwira ntchito zachipatala ndi zipangizo zokwanila; sukulu za mkomba phala zomwe zili ndi zipangizo zokwanila koman-so zoyenerekera zonse; sukulu zapulaimale ndi sekondale zokwanila mogwilizana ndi chiwelengero cha anthu, zokhala ndi zoyenerekera zonse komanso aphunzitsi ophunzila bwino ndi cholinga choti mwa-na aliyense m'Malawi alandire maphunziro abwino osachepera zaka 12; magetsi adzakhale paliponse komanso odalilika; misewu ya pamwamba ndi yaphula; madzi akumwa abwino a m'mipopi; sukulu za umisili ndi maluso osiyanasiyana; ntchito za internet ndi lamya; ndi nyumba zabwino komanso za malata kwa aliyense. Pomwe zonse zofunikila zomwe tazitchulazi tidzazifikire, tizadziwa kuti masom-phenya athuwa tikuwakwaniritsa.

Kuti tikwaniritse masomphen-yawa, pakufunika kuganiza bwino pa chikhalidwe chathu monga kukhala osasankhana mitundu, kukonda dziko lathu, kulimbikila ntchito, kumvera malamulo ndi kukhala odana ndi zaulele.

Tikudziwa kuti palibenso wina yemwe adzatukule dziko lathuli koposa ife eni ake a Malawi. Kotero, sitidzalora kuti munthu wina aliyense atisokoneze zomwe ife tagwirizana. Ife tipita chitsogolo potukula dziko lathu ndi kukhala odzidalira pogwilitsa ntchito mphamvu zathu, zida ndi zachilengedwe zomwe tili nazo m'dziko mwathu mom'muno. Izi ndizimene a Malawi tikufuna ndipo tidzayembekezera a zipani zonse zandale m'dziko muno kuti adzalongosole muma manifesito awo kuti adzakwaniritsa bwanji masomphenya athuwa. Chimodzimodzinso mabungwe onse omwe si a boma ndi a mayiko akunja akufuna kwabwino, adzayenera kulunjika thandizo lawo m'magawo amene ali mu ndondomeko ya masomphenya athu-wa a Malawi 2063.

***Malawi Yemwe Tikumufuna ndi Otheka Ndipo Afika Ndithu!***